**CHICHEWA – *“Where is your home?”***

# NYUMBA YANU ILI KUTI?

Ambili mwa ife tili ndi nyumba, kapena malo amene timawachula kuti ku nyumba kwanga. Sikungafanane ndi kwa ena cifukwa kwa ena kuli katundu wapamwamba, ndipo ndikowoneka bwino, Koma kwanu ndi kwanu ngakhale titapita kutali, timakondwela tikabwelela kunyumba kwathu ngakhale kuti ndikosawoneka bwino, umakondwela nako ku nyumba kwako. Angakhale kuti kumalo kumene unapitako kunali kwa bwino zedi kokongola kuposa kwanu chodziwika ndichoti kumeneko, sikunali kunyumba kwanu kunali kwa eni. Pamene tinali kwa eni cikumbo kumbo cha kwathu chinalipo. Pali chinthu china chimene chimakupangisa kuti ngakhale ukakhale kwina koma umafunabe kunyumba kwako, kwanu ndi kwanu.

## NDIFE ALENDO PANSI PANO

Ndife alendo kuno. Mau a Mulungu amatiwuza kuti ndife alendo ku dziko lapansi lino (1 Petro 2:11; Aheberi 11:13). Malo amene timawacha kuti ndi kunyumba kwathu pansi pano ndi a kanthawi, posachedwa a gumuka



khoma limawazika padenga podontha dontha, mphepo imawomba kulowela pazenera pakhomo, kenako plastala amachoka pang'ono ndi pang'ono pakwatupo pamayamba kusasuka. Palibe nyumba padziko lapansi lino imene ili yokhalisa. Zimasunduka bwinja. Tikawona zoti zungulira timawonadi kuti padziko lino zinthu sizokhalisa zimangodusa angakhale nyumba zathu pansi pano sizokhalisa.

## ALIYENSE MWA NJIRA INA ALI NDI NYUMBA YOKHALITSA

Aliyense mwa ife khaya akudziwa kapena sadziwa ali ndi nyumba yokhalitsa nyumba imeneyi ndi kumene udzapita moyo wako ukatha ku dziko lino lapansi tikamwalira ndikuikidwa m'manda, Miyoyo yathu imapita kwawo kwa muyaya kumene sukakhala mlendo Malo ena kumene ena adzapita kukhala monga kwawo kwa muyaya ndi ku nyanja yamoto ya salifule kumene chilombo ndi mneneri wonyenga ali kumeneko satana ndi onse amene sanalembedwe mu buku la moyo adzaponyedwa kumeneko. Chivumbuluso 20:10-15 mumalawi owopya amoto awa kudzakhala kulira ndi kukuta mano. Awa ndi malo owopya zedi. Osamva onse kwawo ndi kumeneko kulibe wokumvela chisoni kulibe wokutonthoza, adzalaka laka kuti akanamvela mau a uthenga wa bwino wa Yesu Khristu. Malo owopya amoto awa Jehena adzakhala wawo kwa muyaya kwa onse osamva Pakuti onse anacimwa napelewela Aroma 3:23. Malo awa ndi kwawo kwa anthu a chigololo, chiwelewele, opembedza mafano, a nyanga, okhwima, afiti, amatsenga, amene ali ndi udani mumtima mwawo, a njilu akaduka, abodza, oledzela, akuba, achinyengo, osakhulupilika, akupha andewu aulesi onyada okonda za dziko lapansi owopya ndi ankhanza adyela a umbombo, okonda ndalama, okonda zamdziko Agalatia 5:19-21; Chivumbuluso 21:8. Kumeneku ndi kwawo kwa anthu okana kulandira Yesu kuti akhale Mbuye ndi Mpulumutsi wawo, anthu amene sanasambe mwazi wa Yesu Agalatiya 6:7.

Tione m'mene munthu wochimwa amapitila kwawo, kumakhala kwawo cifukwa sanalandile Yesu kukhala Mbuye ndi Mpulumusi wake. Wochimwa amamwalira thupi lake litadzala ndi ululu ndipo moyo wake utadzala ndi mantha kuopa imfa. Kwa iye imfa imafika asakuyembekezela ndipo mwankhanza Zokoma za chimo zatha ndipo zapita. Tsopano mpoto ya uchimo iyenela kulipilidwa Aroma 6:23. Zowopya za jehena zagwila moyo ndi mzimu wa wochimwa pamene alikufa. Angakhale atafuna kuti apemphele, sangathe kulumikizana ndi Mulungu. Azingake akuwopa kuima pa bedi lake ndipo mau awo ndi chuma chimene mwina anachipeza mwa chinyengo sizingathe kumtontoza kapena kuthetsa ululu umene akuwumva, kapena kutalikitsa moyo wake. Ngakhale atayesa kuganizila za Mulungu Satana sangampatse mpata munthu wotere wagwidwa basi. Zonse zimene iye

anazikonda kudziko lino lapansi zimawoneka ngati zikumunyoza angakhale amene anali mbusa wake wa dziko naye akulephela kumtandiza Tsopano amayamba kuzindikila kuti ndikoopya kugwa mdzanja la Yehova. Aheberi 10:31. Amaganiza kuti nthawi imeneyi ali pa bedi akhoza kukonza moyo wake ndi Mulungu koma amawonanso kuti nthawi yatha. Miyanda miyanda ya anthu akumwalira mwamsanga osamdziwa Mulungu Tawuzidwa kuti mfuneni Yehova Yesaya 55:6 m'malo mwa kumva mau a Mulungu mau a chikondi otonthoza pa nthawi imene anali ndi moyo, amadzamva tsono mau awa woweluza Mbuye amene anamkana akumuwuza kuti choka kwa Ine iwe wotembeleledwa pita ku moto umene unakonzeledwa Satana ndi amithenga ake Mateyu 25:41; Aheberi 9:27.

## TIWONE NYUMBA YA BWINO

Munyumba iyi mulibe mdima kulibe usiku mulibe nyali dzuwa silifunika kumeneko cifukwa Ambuye ali komweko Chivumbuluso 22:5. Wina aliyense sanawone kapena kumva kapena kuziganizila zimene Mulungu wakonzela amene amukonda Iye 1 Akorinto 2:9. Palibe chiyankhulidwe cha pansi pano chimene chinganene za ulemelero wa Mulungu ku mwamba Kumeneku ndiko kwao kwa anthu owomboledwa Palibe wochimwa amene akalowe kumwamba chonyansa chili chonse sichikalowa. Okhawo amene maina awo alembedwa mu buku la moyo Buku la mwana wa Nkhosa akalowa Chivumbuluso 21:27. Nyumba iyi sigulidwa ndi ndalama kapena kuyigwilira ntchito. Sungakwele pa makoma ake, palibe zochitika za mumpingo zimene zingakupatse nyumba imeneyi, pali njila imodzi yokha basi ndiko kuzela mwa Yesu Khristu basi. Anati Mnyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu pakuti ndipita kukukonzerani inu malo Yohane 14:2 Yesu ananena za nyumba imene olapa amene mtima ndi moyo wawo ndi zoyela. Anthu ena ali ndi zovala zimene amaganiza kuti akavala ndiye kuti akalowa kumwamba. Pakufunika mtima woyera osati zovala zakunja kuno, tikhale moyo wa chiyero osatsata za dziko.

Tikuonatu kuti tonse ndife ochimwa pamaso pa Mulungu ndipo tili pa ulendo wopita ku jehena, pali chinthu chimodzi choti tichichite tikawulula machimo anthu kwa Mulungu adzasunga pangano lake kwa ife: Adzakhululukira machimo athu ndikutiyelesa 1 Yohane 1:9. Yesu anati ndine kuwuka ndi moyo. Aliyense wokhulupila Ine ngakhale akafa adzakalanso ndi moyo. Aliyense wokhulupila Ine sadzafa Yohane 11:25-26; Yohane 5:24 Imfa singathe kuzunza kapena kupeleka mantha kwa woyera mtima Imfa inagonjesedwa. Chipambano ndi cha tunthu Imfa iwe mphamvu yako ili kuti? Kupambana kwako kuli kuti? Tiyamika Mulungu amene amatipatsa ife kupambana kudzela mwa Yesu Khristu 1 Akorinto 15:54-57.

Munthu amene wakhala moyo ndikuyenda ndi Yesu samaopa imfa. Nthawi yake ya imfa ikakwana amamwalira mopanda kuvutisa amapita mwa mtendere. Mtumwi Paulo anati Koma ndipanidwa nazo ziwirizi pokhala naco colakala ca kucoka kukhala ndi Khristu ndiko kwabwino koposa posatu Afilipi 1:23. Mkhristu amafunitsitsa kuzaona nkhope ya Yesu amene anamufela pa mtanda. Mzimu woyera amakukumbutsa za mau a Yesu Yohane 14:1-4. Tiyime pang'ono tiwone m'mene mkhristu amanyamukila pa ulendo wopita kwawo. M'malo mwa imfa yochititsa mantha, mngelo kapena wamithenga wa Ambuye amakhala akudikila kuti amupelekeze woyera mtima kwawo kwa Mulungu. Moyo ndi mzimu wa munthu zimachoka mutupi ndikulisiya, ndipo amapita kukalowa pazipata zakumwamba kwa amene anamufela. Amalandilidwa mwa chimwemwe napatsidwa moni ndi Mbuye wake ndi mau awa Mat 25:21. Satana alibenso mphamvu pa iye, Chiv. 14:13. Muchite zimene mwana wolowelera anachita, pamene anawona chizunzo pamoyo wake anati ndinyamuka ndipite kwa Atate Luka 15:18. Peleka moyo wako kwa Yesu, tsopano lomweli usacedwe. Pamene ulipo gwada pansi uvomeleze kuti ndiwe wochimwa akukhululukire akutsuke ndi mwazi wake wamtengo wapatali Mulandileni Yesu tsopano Njila yaku jehena ya Satana muyisiye. Muyambe ulendo wopita kwanu kumwamba.

M.R. GSCHWEND

---

The popular "Heart Book" with its soul-saving message is obtainable in over 500 languages. Many have found salvation even just by looking at the pictures. **Our Heart of Man Book can now be downloaded in 480 different languages onto cell phones, tablets, etc from our website www.angp-hb.co.za**

Kindly write to us if you are able to assist us with further translations of our free Gospel literature, informing us of the language into which you could translate this Gospel literature. Your assistance would be appreciated.

If you have found salvation in Christ, or have been otherwise blessed through our Gospel literature, please let us know. We would like to thank God with you, and remember you further in our prayers.

For **free** Gospel literature, books and tracts in over 540 languages, write to:


**E-MAIL: info@angp.co.za**

**ALL NATIONS GOSPEL PUBLISHERS**

**P.O. Box 2191, PRETORIA, 0001, R.S.A.**

(A Gospel Literature Mission financed by donations)

(Reg. No. 1961/001798/08)